NAMBALA YA MAYESO: ______________________________________ SUBJECT NUMBER: P078

**MOUNTAIN VIEW ZONE EXAMINATIONS BOARD**
**2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE**

**MOCK EXAMINATIONS**

**CHICHEWA**

**(100 MALIKISI)**

**SUBJECT NUMBER P 078**

**TSIKU: ____________________________** **TIME ALLOWED: 01:00 – 03: 15**
**(2 hrs 15min)**

**DZINA LANU: _______________________________________________________________**

(Surname First)

**DZINA LA SUKULU YANU: ___________________________________________________**

**MALANGIZO.**

1. **Onetsetsanani kuti pepala iri liri ndi masamba asanu ndi atatu.**
2. Lembani **dzina lanu** pamwamba pa pepalali.
3. Pepala iri liri ndi magawo **anayi** gawo **A, B, C** ndi **D.**
4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu gawo **B, C** ndi **D**.
5. Lembani mafunso mu gawo **B, C, D** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lirilonse .
6. Yankhani mafunso a mugawu **D** pozunguliza lembo lokhoza pa funso.
7. Chongani funso lomwe mwayankha mu tebulo lomwe mwapatsidwa**.**
8. Perekani kwa okuyang'anirani mayeso pepalali nthawi ikakwana.

| Question Number | Tick if answered | Do not write in these columns | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 7 - 10 | | | |
| 11 - 15 | | | |
| 16 - 20 | | | |
| 21 - 25 | | | |
| 26 - 30 | | | |
| 31 - 35 | | | |
| 36 - 40 | | | |
| 41 - 44 | | | |
| | | | |

**© 2024 STANDARD 8 MOCK EXAMINATIONS.** **Turn over**

**GAWO A (MALIKISI 30)**

**LANGIZO:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa.

Sankhani Chimangirizo kapena kalata mawu a m'chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere100 komanso asapitilire 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu woti MATENDA OTSEKULA M'MIMBA
   Mwa zina tsatani izi polemba.

   **Ndime yoyamba**

   - Tchulani dera lomwe mukukhala.
   - Delari lazunguliridwa ndi midzi ingati?
   - Tchulani ena mwa matenda otsekula m'mimba omwe amafala m'derali.

   **Ndime yachiwiri**

   - Tchulani njira zomwe matendawo akufalira.
   - Fotokozani m'mene anthu angapewere matendawo.
   - Kodi matendawo amafala kwambiri nthawi iti?

   **Ndime yachitatu**

   - Pempho lanu ndi lotani ku likulu la za umoyo pa matendawo.
   - Ndi chiopsezo chanji chomwe matendawo abweretsa ku dera lanulo.

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa nzanu yomufotokozera za malonda osiyanasiyana omwe amachitika m'dera lanu.
   Mwa zina tsatani izi polemba.

   **Ndime yoyamba**
   - Tchulani dera limene mumachokera.
   - Tchulani matenda osiyanasiyana omwe anthu amachita.
   - Tchulani ina mwa misika yozungulira dera lanu komwe anthu

   **Ndime yachiwiri**
   - Fotokozani kufunika kwa malonda osiyanasiyanawo
   - Fotokozani mavuto omwe anthu ochita malondawo amakumana nawo

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani m'mene anthu a malondawo angathetsere mavuto awowo pochita malonda.
   - Perekani malangizo kwa ochita malonda kuti apeze phindu lochuluka.

**GAWO B: (MALIKISI 20)**

Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

Pa mudzi pa Mbiriyamveka padali mlenje wina wotchuka kwambiri wotchedwa Chirikumanja.anthu m'mudzimo adamupatsa dzinali chifukwa akapita ku ulenje samabwerako manja ali m'khosi. Iye ankatchera misampha ya chigwenembe, ankayenda ndi legeni, mipaliro ndi mauta popita ku liwamba. Ngakhale mlenjeyu ankapha nyama tsiku ndi tsiku, adali kanga ndiwamba.
Chirikumanja adalibe nzake weni wenimmudzi muja. Iye sankatenga nawo mbali pa zochitika za pa mudzi monga pa maliro, paukwati, pazisangalaro ngakhalenso chitukuko.

Tsiku lina kudamveka mfuwu kunyumba ya Chirikumanja. Iye adakuwa ngati mwana kuitana anthu kuti adzamuthandize. Koma anthu onse anali duu! M'makomo mwawo. Ngakhale iye adakuwa mopitiriza komabe sizinaphule kanthu. Chirikumanja adagwira njakata. Njoka ya Nsato ndi yomwe idalowa m'nyumba mwake ndipo ankaitana anthu kuti azamuthandize kupha chinjokacho.
Chifukwa cha mantha, iye adakhala masiku atatu akugona palumbe.

Amfumu atamva za nkhaniyo adamva chifundo ndipo adaitana Sing'anga Kalikokha kuti apite limodzi ku nyumba ya mkuluyo. Sing'anga Kalikokha atafika adawaza mtera mnyumbamo ndipo ka nthawi pang'ono chinjokacho chidatuluka nkuthawa. Chirikumanja ataona iziadatsimikizira amfumu kuti sazayerekezanso kumapanga zinthu yekha chifukwa adadziwa kuti kuyenda awiri si mantha.

**MAFUNSO (20 MALIKISI)**

a) Mlenje wotchuka ankachokera pa mudzi wanji?
________________________________________ (malikisi 1)

b) Kodi mlenjeyo adatchuka chifukwa chani?
________________________________________ (malikisi 1)

c) Tchulani zipangizo ziwiri zokha zomwe mlenjeyo ankatenga popita kuuzimba.
________________________________________
________________________________________ (malikisi 2)

d) Mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani mlenjeyo adalibe nzake weniweni m'mudzi muja. Perekani zifukwa ziwiri zokha.
________________________________________
________________________________________ (malikisi 2)

e) Pezani mikuluwiko mu nkhaniyi yomwe matanthauzo ake ndi awa:
   i. Kugona panja usiku onse osafunda ____________________ (malikisi 2)
   ii. Kusowa chochita ____________________ (malikisi 2)
   iii. Munthu omana ____________________ (malikisi 2)

f) Perekani matanthauzo a mawu awa:
   i. Sizinaphure kanthu ____________________ (malikisi 1)
   ii. Mtera ____________________ (malikisi 1)

g) Kodi ndani adamvera chifundo Chirikumanja?
________________________________________ (malikisi 1)

h) Kodi chidapangitsa nchiyani kuti Chirikumanja ayambe kupezeka mmagulu a mmudzi?

i) ____________________________________________________________(malikisi 1)

j) Perekani mutu wa nkhaniyi.

____________________________________________________________ (malikisi 1)

**GAWO: C (MALIKISI 10)**

Yankhani mafunso awiri m'gawoli.

Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

Dodolido : Zikomo! Zikomo, zikomo kuno!

Dolika : Ee! Alowe apongozi. Monitu, nanga muli bwanji?

Dodolido : Ine ndiribwino, sindidziwa inu mulibwanji? Ndangomva kuti atsibweni simoyo!

**MAFUNSO.**

1. Ndi malonje anji amenewa?

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
2. Malonjewa akuchitikira kuti?

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
3. Mawu oti "simoyo" akutanthauzanji?

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)

4. Tchulani njira imodzi yopewera matenda otsekula mmimba.

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
5. Perekani njira imodzi ya makolo yofalitsira mauthenga.

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)

Pangani ziganizo ndi mawu awa:

a. zake

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
b. bungwe

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
c. ndipo

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)

d. wadzitho

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)
e. chete

   ____________________________________________________________ (malikisi 1)

**GAWO D (MALIKISI 40)**

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) mmafunso otsatirawa.

**Mafunso 6-10** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo

m'ziganizo Zotsatirazi.

6. Choka! Mwana waulesi iwe.
   - A. Dzina C. Mfotokozi
   - B. Mneni D. Mfuwu
7. Wandibera limene ndagula.
   - A. Mneni C. Dzina
   - B. Mlowammalo D. Mlumikizi
8. Alembi athu awa ndi a Ntchona.
   - A. Mlowammalo C. mneni
   - B. Mfotokozi D. Muonjezi
9. Icho ndi choipa.
   - A. Mlumikizi C. Mperekezi
   - B. Mfotokozi D. Mneni
10. Mtima suvala nsanza.
    - A. Mneni C. Mfotokozi
    - B. Dzina D. mlowammalo

**Mafunso 11-15** Sankhani mitundu ya nthawi ya aneni.

11. Mwana akuphunzira masamu.
    - A. Yakale
    - B. Yakale yathayi
    - C. Yatsopano yopitilira
    - D. yatsopano
12. Elube adalemba mayeso.
    - A. Yamtsogolo
    - B. Yakale
    - C. Yakale yathayi
    - D. Yam'tsogolo yathayi.
13. Wagwidwa akuba matemba.
    - A. Yatsopano
    - B. Yam'tsogolo
    - C. Yakale
    - D. Yatsopano yopitilira
14. Ine ndizakhoza mayesowo.
    - A. Yam'tsogolo
    - B. Yatsopano
    - C. Yakale
    - D. Yatsopano yathayi
15. Anyamata azizagwira ntchito m'migodi.
    - A. Yatsopano yathayi
    - B. Yam'tsogolo yopitilira
    - C. Yatsopano
    - D. Yakale

**Mafunso 16-20** Sankhani gulu la mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

16. Galimoto yanga yatchona.
    - A. Ga-Li C. I-Zi
    - B. Li-Ma D. A-Ma
17. Pumbwa wakodwa paulimbo.
    - A. A- Pu C. Chi-Zi
    - B. Mu-A D. Pu-A
18. Wagula lamba wosalimba.
    - A. Li-Ma C. Mu-A
    - B. Mu-mi D. I-Zi
19. Amayi anga apita kumunda.
    - A. Mu-Mi C. U-Ma
    - B. Mu-A D. Ku-Pa-Mu
20. Gulu loyimba nyimbo labwera.
    - A. I-Zi C. Gu-Lu
    - B. Li-Ma D.Lu-A

**Mafunso 21-25** Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

21. Amayi ake ndi apakamwa poola
    - A. Wodwala C. Wolongolora
    - B. Wochezeka D. Achibwana
22. Achemwali akwatiwa ndi kathyali.
    - A. Wakuba C. Wonama
    - B. Wolemera D. Wachikulire

23 Ana oyera m'maso amamenyedwa

A. Amwayi C. Woyerekedwa

B. Aakulu maso D. Atsoka

23. Wagula mondokwa ku nsika.

A. Chimanga C. Mtedza

B. Chinangwa D. Mbatata

24. Abambo ake ndi achimasomaso.

A. Amitala
B. Wokwatirakwatira
C. Achiwerewere
D. Wogwilirira ana

**Mafunso 26-30** Sankhani matanthauzo a zining'a zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi.

25. Nalitchowa anayabwidwa chitedze.

A. Adapalamula mavuto
B. Adatola ndalama
C. Adatenga matenda
D. Adatenga mbiri

26. Angozo adaluma mano dzulo.

A. Adamwalira C. Aziluma

B. Adwalika D. Avulala

27. Mnyamata uyu ndi mphungu sataya nthenga.

A. Wamakani C. wauve

B. Womana D. Waulesi

28. Amayi awa adugulura khasu ndi kumbuyo.

A. Kusabereka C. Kusowa banja

B. Kubereka D. ulesi

29. M'nyamata uyu ndi kamwendo njira.

A Wamatama C. woyendayenda

B Wodwaladwala D. Wakuba

**Mafunso 31-35** Sankhani chachimuna cha mawu omwe atsekedwa kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

30. Tapatsidwa misoti iwiri ndi amalume.

A. Mkota C. Mzambwe

B. Atambala D. Chipsolopsolo

31. Iye adabwera ndi apongozi ake.

A. Atengwa C. Akazi

B. Amayi D. Atatavyala

32. Mtengwa uja wabwera.

A. Ntchembere C. Mpongozi

B. Mkamwini D. Mfumu

33. Amzakazi angapo athawa.

A. Amfumu C. Akapolo

B. Anyakwawa D. Msona

34. Ntchembere zasonkhana pansi pa mtengo.

A. Ndoda C. Tonde

B. Mfumu D. Tambala

**Mafunso 36-40** Sankhani msintho wa aneni oyenera omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo

35. Wakuba wamangiririridwa pa mtengo.

A. Womchititsa
B. Wochitirana
C. Wochitiridwa
D. Wotsutsa

36. Mphaka <u>watsekula</u> zenera.
    - A. Wotsutsa
    - B. Wochitidwa poyera
    - C. Wochitiridwa
    - D. Wochititsa
37. Mkeka <u>walukika</u> bwino.
    - A. Wochitidwa poyera
    - B. Wochitidwa m'chibisira
    - C. Wochititsa
    - D. Wochitidwa monyazitsa
38. Mbuzi ya a Bengo <u>yaphedwa</u>.
    - A. Wochitiridwa
    - B. Womchititsa
    - C. Wochitidwa poyera
    - D. Wotsutsa
39. Galu <u>waphedwa</u> pamsewu.
    - A. Wotsutsa C. Wochitiridwa
    - B. Wonyazitsa D. Wochititsitsa

**Mafunso 41-45** Tchulani mtundu wa nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo.

40. Abigelo akuwerenga buku <u>lomwe adagula dzana</u>.
    - A. Yamfotokozi C. Yamuonjezi
    - B. Yadzina D. Yamneni
41. Magireti amayenda <u>ngati akuvina.</u>
    - A. Yadzina C. Yamuonjezi
    - B. Yamfotokozi D. Yamlowam'malo
42. Adandiuza <u>kumene amaphunzira</u>.
    - A. Yamfuwu C. Yadzina
    - B. Yamperekezi D. Yamuonjezi
43. Mtsikana <u>amene wakhala apayu</u> ndi waulesi.
    - A. Yamuonjezi C.Yamwini nkhani
    - B. Yadzina D. Yamfotokozi
44. <u>Zoti adzabweranso kuno</u> sizidziwika.
    - A. Yapamthera nkhani
    - B. Yadzina
    - C. Yamfotokozi
    - D. Yamuonjezi

## MAFUNSO ATHERA POMWEPA!!!!